# KALAMBO ZONE EXAMINATIONS BOARD

## 2024 PRIMARY LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Thursday, 29 February, 2024** **Subject Number: PO32**

**Time Allowed: 2hrs-15mins//1:00-3:15PM**

**Dzina lanu** :________________________________________

**Dzina la sukulu** : ________________________________________

**<u>Malangizo:</u>**

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba otsindikizidwa **asanu ndi anayi.**
2. Pepala ili lili ndi **magawo anayi: Gawo A,B,C** ndi **D**
3. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba patsamba lino.
4. Lembani chimangilizo kapena kalata mu Gawo A ndipo muyankhe mafunso once mu **Gawo B,C ndi D**
5. Lembani yankho la mu **Gawo A** pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu Gawoli
6. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.
7. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza pafunso lililonse.
8. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mu bokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
9. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso (imvjireta) pepala lonseli nthawi ikakwan.

| **Funso** | **Chongani Zomwe mwayankha** | **Muno musalembemo** | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

***Tsekulani paseri…………***



**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518

## GAWO A

**Langizo:** Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa Chimangirizo kapena wa Kalata. Mawu a Chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150.**

1. **Lembani Chimangirizo pa mutu uwu:**

   **TSIKU LOSAIWALIKA**
   **Mwazina tsatirani izi polemba chimangirizo chanu.**

   ***Ndime Yoyamba***
- Kodi lidali tsiku liti ndiponso nthawi yanji?
- Kudachitika zotani?
- Nanga zidachitikira kuti?

   ***Ndime Yachiwiri***
- Momwe zochitikazo zidakukhudzilani
- Mudatengapo gawo lanji pa zochitikazo?

   ***Ndime Yachitatu***
- Zinthu zomwe zidachititsa kuti tsikuli likhale losaiwalika

## KAPENA

2. **Lembani kalata kwa m'bale wanu yemwe amakhala kutali ndinu yomufotokozera chitukuko chomwe chachitika ku mudzi wanu.**

   **Mwa zina tsatirani izi polemba:**

   ***Ndime yoyamba***
- Fotokozani chitukuko chomwe chachitikacho
- Tsiku, mwezi ndi chaka chomwe chitukukocho chidayamba.

   ***Ndime yachiwiri***
- Momwe chitukukocho chinayambira
- Fotokozani zomwe inu mudachitako pachitukukopo
- Fotokozani momwe chitukukocho chatukulira mudzi wanu

   ***Ndime yachitatu***
- Zomwe mukuchita kuti chitukukocho chipitilire
- Momwe mungamulimbikitsire m'bale wanuyo kuti abwere kumudziko.



**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518

**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518

## GAWO B (MALIKISI 20): KUMVETSA NKHANI

**Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawa:**

Idali nthawi ya masana ophunzira atatsala pang'ono kuweruka. Mphunzitsi adayamba kukambirana ndi ophunzira ake nati "ana inu, ndakhala nanu pa chaka chonse ndipo ndaona kuti ndinu ana abwino, ndinu ana aulemu, omvera ndi olimbikira sukulu makhalidwe otere ndi omwe ife timakondwera nawo. Pa chifukwa chimenechi ndaganiza kuti ndikuchitireni kanthu kena " ophunzira onse adasangalala ndi nkhaniyo ngakhale samadziwa chimene mphunzitsi wawo amkatanthauza. Mwana wina wotchedwa Chifuniro adafunsa aphunzitsi nati: "Kodi kanthu mukunenako n'chiyani? Mphunzitsiyo adamuyang'anitsitsa m'nyamatayo ndi chidwi ndipo adamwetulira. Atatero adatsekula pakamwa nati: "ndikuganiza kuti tidzakhale ndi phwando tikamadzatsekera sukulu" ophunzira onse adaomba m'manja nadumpha kusonyeza chisangalalo chawo.

Ophunzira adafunsa mafunso mphunzitsiyo zokhudza phwandoli chifukwa ambiri aiwo kudali koyamba kudzachita phwando la mtundu woterewu. Wophunzira wina dzina lake Fatsani adafuna kudziwa momwe adzapezere ndalama yokonzekera phwando la kalasi yonse. Iye adafotokoza kuti ali mu Sitandade 5, mphunzitsi wawo adawauza kuti adzakhala ndi phwando potsekera sukulu koma zidalephereka chifukwa chosowa ndalama. Amzake onse mkalasimo adaseka phwetephwete koma mphunzitsiyo adadziwa chomwe mnyamatayo amatanthauza.

Iye adauza ophunzira kuti asadandaule ndi nkhani ya ndalama chifukwa khotekhote ngwanjira kwaloza mtima nkomweko. Atatero adagwirizana tsiku ndi nthawi yomwe phwandolo lidzachitike.

**MAFUNSO**

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

a. Kodi idali nthawi yanji imene mphunzitsi amkakambirana ndi ophunzira:
______________________________ **(malikisi 2)**
______________________________

b. Perekani makhalidwe atatu a ophunzira a mkalasi?
______________________________ (**malikisi 3)**
______________________________

c. Kodi kanthu komwe mphunzitsi amkafuna kuwakonzera ophunzira aja kadali chiyani?
______________________________ (**malikisi 2)**
______________________________

d. N'chifukwa chiyani ophunzira adaomba m'manja nadumpha?
______________________________ (**malikis 2)**
______________________________

e. Tchulani dzina la wophunzira yemwe adafuna kudziwa za momwe angapezere ndalama za phwando.
______________________________ (**malikisi 2)**

f. Perekani matanthauzo amawu awa:
(i). Adaseka phwetephwete:______________________________ (**malikisi 2)**



©KAZEB
@MBALU:0999816877/0888467518

(ii). Khotekhote ngwanjira kwaloza mtima n'komweko:________________________________________
________________________________________________________________________________(**malikisi 2)**

g. Pezani mawu mnkhaniyi omwe akufanana m'matanthauzo ndi awa:
   (i).Chilumika:___________________________________________________________(**malikisi 2)**
   (ii).Madyelero:__________________________________________________________(**malikisi 2)**

h. Tchulani mutu woyenera wa nkhaniyi. ______________________________________(**malikisi 1)**

**GAWO C: (MALIKISI 10)**

**Yankhani mafunso awiri omwe ali m'gawoli:**

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsarirawa:

   Zikomo anamalira nonse, zikomo gogo Thupilo. Nthawi ino tikufuna tiyambe mwambo wathu. Tiyeni tonse tikhale chete kuti tipereke ulemu wotsiriza pa mwambo komanso timvane.

   **Mafunso.**

   a. Kodi angayankhule mawuwa ndani? (**malikisi 1)**
   ________________________________________________________________________
   b. Nanga angawayankhule pamwambo wanji? **(malikisi 1**)
   ________________________________________________________________________
   c. Perekani cholakwika m'malonjewa ndipo muchikonze polemba chiyerekezo cahke (**malikisi 2)**
   ________________________________________________________________________
   ________________________________________________________________________
   d. Kodi mukamayankhula ndi munthu wamkulu mumayenera kutani**?** **(malikis 1)**
   ________________________________________________________________________



**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518

5. **Kupanga ziganizo**
   **Pangani ziganizo zomweka bwino ndi mawu awa:**

   a. Chumba (malikisi 1)

   ______________________________________________

   ______________________________________________

   b. Mkoko (malikisi 1)

   ______________________________________________

   ______________________________________________

   c. Pakati (malikisi 1)

   ______________________________________________

   ______________________________________________

   d. Ponda (malikisi 1)

   ______________________________________________

   ______________________________________________

   e. Amene (malikisi 1)

   ______________________________________________

   ______________________________________________



**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518

**GAWO D (MALIKISI 40)**
**Zungulizani lembo lokhoza A,B,C kapena D. Mafunso 6 mpaka 10. Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:**

6. Mwana wanga sakonda kudya nsima
   A. Dzina
   B. Mlowam'malo
   C. Mfotokozi
   D. Mneni

7. Achimwene aphera iweyo mbuziyi
   A. Muonjezi
   B. Mfotokozi
   C. Mlowam'malo
   D. Dzina

8. Angozo ndi mphunzitsi wabwino.
   A. Mlumikizi
   B. Mperekezi
   C. Mfotokozi
   D. Mneni

9. Mkazi wake wapita usiku.
   A. Mvekero
   B. Mneni
   C. Muonjezi
   D. Mfuwu

10. Nditengabe mwana wangayu ngakhale ukwiye.
    A. Mneni
    B. Mlumikizi
    C. Mperekezi
    D. mgwirizanitsi

**Mafunso 11 mpaka 15. Sankhani mitundu ya a fotokozi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:**

11. Msungwana wokongola wabwera
    A. Wamakhalidwe
    B. Wamaonekedwe
    C. Woloza
    D. Waumwini

12. Akazi a chimalawi ndi aulemu.
    A. Wamgwirizano
    B. Waumwini
    C. Wamwinimwini
    D. Wachiwerengero

13. Buku lomwe labedwalo ndi langa.
    A. Wamgwirizano
    B. Woloza
    C. Wamaonekedwe
    D. Wamakhalidwe

14. Ndikupatsani mbuzi zitatu zokha.
    A. Waumwini
    B. Wofunsa
    C. Wochuluka
    D. Wachiwerengero

15. Ana awa akugona.
    A. Wamwinimwini
    B. Wamakhalidwe
    C. Woloza
    D. Wofunsa

**Mafunso 16-20: Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo:**

16. Chivululu
    A. Nthutumba
    B. Chiboda
    C. Matumbo
    D. Kapamba

17. Wogunata
    A. Wotsatira
    B. Wofuntha
    C. Chidzete
    D. Wochenjera

18. Chisangalalo
    A. Khirisimasi
    B. Chaka
    C. Chikondwelero
    D. Chilumba

19. Chipala
    A. Lezala
    B. Dzala
    C. Makala



©KAZEB
@MBALU:0999816877/0888467518

D. Phulusa

20. Chilumba
    A. Mtunda
    B. Chisumbu
    C. Dera
    D. Nyimbo

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:**

21. Apunthwa katatu achimwene ako.
    A. Dzina loitanila
    B. Mwininkhani
    C. Pamtherankhani
    D. Mtsirizitsi

22. Tigula galimoto chaka chino.
    A. Mtsirizitsi
    B. Mwininkhani
    C. Pamtherankhani
    D. Dzina lapadera

23. Zione, tabwera kuno.
    A. Dzina loitanira
    B. Dzina lapadera
    C. Mwininkhani
    D. Mtsirizitsi

24. Joni si mnyamata wabwino.
    A. Mwininkhani
    B. Pamtherankhani
    C. Loitanira
    D. Mtsirizitsi

25. Pamunda pasonkhana anthu ambiri.
    A. Kuitanila
    B. Kusonyeza malo
    C. Dzina lapadera
    D. Pamtherankhani

**Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani matanthauzo a mizimbayitso yotsatirayi?**

26. Mwana wapatuka.
    A. Wasiya njira
    B. Wathawa
    C. Wanyera
    D. Wabisala

27. Mayi wapita padera
    A. Wabala mwana wakufa
    B. Wanama
    C. Wamwalira
    D. Wasokera

28. Nambewe ndi nkhwangwa.
    A. Wokongola
    B. Wosaoneka bwino
    C. Wazitchito
    D. Wophunzitsa

29. Anyamatawa amagona pamphepo.
    A. Amagona panja
    B. Alibe zofunda
    C. Alibe banja
    D. Mnyumba ndi mozizira

30. Abambo atisiya dzulo
    A. Amwalira
    B. Apita
    C. Athawa banja
    D. Akudwala

**Mafunso 31 mpaka 35. Sankhani chachimuna cha mawu awa:**

31. Msoti
    A. Tonde
    B. Tambala
    C. Nkhunda
    D. Chipsolopsolo

32. Mdzakazi
    A. Mjomba
    B. Ndoda
    C. Zaka
    D. Kapolo

33. Nzidzi
    A. Chipsolopsolo
    B. Mfule
    C. Kadzidzi
    D. Gocho



**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518

34. Nankungwi
    A. Mjomba
    B. Mkamwini
    C. Wakunjira
    D. Agogo

35. Mfumukazi
    A. Muphwa
    B. Mfumu
    C. Nyakwawa
    D. Nduna

**Mafunso 36 mpaka 40. Sankhani mikuluwiko yotsutsana ndi yotsatirayi:**

36. Kanthu nkako uvundukula nupenya
    A. Zathu salowa m'khola
    B. Tsabola wakale sawawa
    C. Pakadafunda padajiwitsa galu
    D. Wakufa sadziwika

37. Tinkanena anathera msiizi.
    A. Bongololo sadzolera mafuta pagulu
    B. Khoswe wapatsindwi adaulula wapadzala
    C. Tsabola wakale sawawa
    D. Ichi chakoma ichi chakoma pusi adagwa chagada

38. Kuona maso ankhono nkudekha
    A. Mphechepeche mwa njovu sapita kawiri
    B. Mwana wang'ona sakulira dziwe limodzi
    C. Wosoka mphasa sagonera zidutswa
    D. Ndionetsetse adathetsa nkhosa

39. Chibwereza chidaphetsa kunda.
    A. Zengerezu adalinda kwawukwawu
    B. Mphini yobwereza ndiyomwe imatumba
    C. Ndapakonda adasiya m'khonde
    D. Njuchi zikachuluka siziyika uchi

40. Mwala wogubuduzika sumera ndere
    A. Pamodzipamodzi padaoletsa dzungu
    B. Muvi woyang'anira suchedwa kugwa m'maso.
    C. Woluka msengwa adyera m'chipapa
    D. Wokaona nyanja adakaona ndi mvuwu zomwe.

**Mafunso 41 mpaka 45. Sankhani mitundu ya nthambi ya chiganizo zosayima pazokha zomwe ziri ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:**

41. <u>Zakuti adyera nyama</u> sizachilendo.
    A. Yoima payokha
    B. Ya muonjezi
    C. Ya dzina
    D. Ya mfotokozi

42. Kumudzi <u>komwe ndinabadwira</u> ndi kuno
    A. Ya mfotokozi
    B. Ya dzina
    C. Yoyima payokha
    D. Ya muonjezi

43. Iye akuyenda <u>ngati watopa.</u>
    A. Ya dzina
    B. Yoima payokha
    C. Ya mfotokozi
    D. Ya muonjezi

44. Chimwemwe wawerenga buku <u>lomwe adagula dzulo.</u>
    A. Ya dzina
    B. Ya mfotokozi
    C. Ya muonjezi
    D. Yoima payokha

45. Anthu akusakaza mitengo <u>ngati mawa sadzaifuna.</u>
    A. Ya muonjezi
    B. Ya dzina
    C. Yoima payokha
    D. Ya mfotokozi

***Mafunso athera pano!!!***



**©KAZEB**
@MBALU:0999816877/0888467518